


# Thandizo Lochokera Kumwamba

Bukhuli ndi laulere —
Siligulitsidwa

Lolembedwa ndi Watson Goodman

**"THANDIZO LOCHOKERA KUMWAMBA" ndi mavesi a Malembo olengedwa molingana ndi nkani zake, kuchokera m'Baibulo. Ndikhulupilira kuti ndimanga yamphamvu ya Malembo ndilo Baibulo.**

**Mau A Mulungu achokera kumwamba ndipo mosakayikira amathandiza mitima yakumva njala ndi ludzu la chilungamo. Pamene munthu atembenuka mtima, nasiya zoipa zake, naitana Ambuye Yesu Kristu kuti akhale m'mtima mwake, nakhulupilira ndi mtima wake wonse mwa Yesu Kristu monga Mpulumutsi wake, Ambuye amazionetsera yekha kwa wokhulupilirayo napatsa mtendere ndi chimwemwe kwa iye. Izi ndinaziona mu 1937, ndipo kuchokera apo sindinasiyanso chiyanjanochi chodabwika chi ya mwa Ambuye. Ndikufulumizani kuti mugonjere kwa Iye TSO-PANO kuti akhale Ambuye ndi Mpulumutsi wanu, ngati simunagonjere kwa Iye kale. —Watson Goodman (1920-2002)**

---

Scripture text reprinted from the Bible in Chichewa by permission of United Bible Societies Africa Regional Centre, Nairobi, Kenya.

### Aroma 5:8

Koma Mulungu atsimikiza kwa ife cikondi cace ca mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife cikhalire ocimwa, Kristu adatifera ife.

### Yohane 13:1

Koma pasanafike phwando la Paskha, Yesu, podziwa kuti nthawi yace idadza yakucoka kuturuka m'dziko lino lapansi, kunka kwa Atate, m'mene anakonda ace a Iye yekha a m'dziko lapansi, anawakonda kufikira cimariziro.

### Cibvumbulutso 1:5

Ndi kwa Yesu Kristu, mboni yokhulupirikayo, wobadwa woyamba wa akufa, ndi mkulu wa mafumu a dziko lapansi. Kwa Iye amene atikonda ife, natimasula ku macimo athu ndi mwazi wace.

### Yeremiya 31:3

Yehova anaonekera kwa ine kale, ndi kuti, Inde, ndakukonda iwe ndi cikondi cosatha; cifukwa cace ndakukoka iwe ndi kukukomera mtima.

### Yohane 3:16

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha.

### Yohane 14:9, 10a

Yesu ananena naye, Kodi ndiri ndi inu nthawi yaikuru yotere, ndipo sunandizindikira, Filipo? Iye amene wandiona Ine waona Atate; unena iwe bwanji, Mutionetsere Atate? Sukhulupirira kodi kuti ndiri Ine mwa Atate, ndi Atate ali mwa Ine?

### I Timoteo 3:16

Ndipo pobvomerezeka, cinsinsi ca kucitira Mulungu ulemu ncacikuru: Iye amene anaonekera m'thupi, anayesedwa wolungama mumzimu, anapenyeka ndi angelo, analalikidwa mwa amitundu, wokhulupiridwa m'dziko lapansi, wolandiridwa m'ulemerero.

### Yohane 1:1, 14

Paciyambi panali Mau, ndipo Mau anali kwa Mulungu, ndipo Mau ndiye Mulungu. . . Ndipo Mau anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife, ndipo tinaona ulemerero wace, ulemerero wonga wa wobadwa yekha wa Atate, wodzala ndi cisomo ndi coonadi.

### Mateyu 1:22, 23

Ndipo zonsezi zinakhala kuti cikacitidwe conenedwa ndi Ambuye mwa mneneri, ndi kuti, Onani namwali adzaima, Nadzabala mwana wamwamuna, Ndipo adzamucha dzina lace, Emanueli; ndilo losandulika, Mulungu nafe.

### I Yohane 4:15

Iye amene adzabvomereza kuti Yesu ali Mwana wa Mulungu, Mulungu akhala mwa iye, ndi iye mwa Mulungu.

### Luka 1:35

Ndipo mngelo anayankha, nati kwa iye, Mzimu Woyera adzafika pa iwe, ndi mphamvu ya Wamkulukulu idzakuphimba iwe: cifukwa cacenso Coyeraco cikadzabadwa, cidzachedwa Mwana wa Mulungu.

### Akolose 2:9

Pakuti mwa Iye cikhalira cidzalo ca Umulungu m'thupi.

### Mateyu 17:5

Akali cilankhulire, onani, mtambo wowala unawaphimba iwo: ndipo onani, mau alikunena mumtambo, Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa, mwa iyeyu ndikondwera, mverani Iye.

### Yesaya 9:6

Pakuti kwa ife mwana wakhanda wabadwa, kwa ife mwana wamwamuna wapatsidwa; ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa lace, ndipo adzamucha dzina lace Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu wamphamvu, Atate Wosatha, Kalonga wa mtendere.

### Yohane 11:25

Yesu anati kwa iye, Ine ndine kuuka ndi moyo: wokhulupirira Ine, angakhale amwalira, adzakhala ndi moyo.

### Yohane 13:13

Inu mundicha Ine Mphunzitsi, ndi Ambuye: ndipo munena bwino; pakuti ndine amene.

### Yohane 8:58

Yesu anati kwa iwo, Indetu, indetu, ndinena kwa inu, asanayambe kukhala Abrahamu ndipo Ine ndiripo.

### Yohane 9:5

Pakukhala Ine m'dziko lapansi, ndiri kuunika kwa dziko lapansi.

### Yohane 8:23

Ndipo ananena nao, Inu ndinu ocokera pansi; Ine ndine wocokera Kumwamba; inu ndinu a dziko lino lapansi; sindiri Ine wa dziko lino lapansi.

### Yohane 6:35

Yesu anati kwa iwo, Ine ndine mkate wamoyo; iye amene adza kwa Ine sadzamva njala, ndi iye amene akhulupirira Ine sadzamva ludzu nthawi zonse.

### Yohane 10:7

Cifukwa cace Yesu ananenanso nao, Indetu, indetu, ndinena ndi inu, Ine ndine khomo la nkhosa.

### Mateyu 14:19-21

Ndipo Iye analamulira makamu a anthu akhale pansi pamaudzu; ndipo Iye anatenga mikate isanuyo ndi nsomba ziwirizo, ndipo m'mene anayang'ana kumwamba, anadalitsa, nanyema, napatsa mikateyo kwa ophunzira, ndi ophunzira kwa makamuwo. Ndipo anadya onse, nakhuta; ndipo anatola makombo otsala, mitanga khumi ndi iwiri yodzala. Ndipo anadyawo anali amuna monga zikwi zisanu, kuwaleka akazi ndi ana.

### Luka 5:4-6

Ndipo pamene Iye analeka kulankhula, anati kwa Simoni, Kankhira kwa kuya, nimuponye makoka anu kukasodza. Ndipo Simoni anayankha, nati, Ambuye, tinagwiritsa nchito usiku wonse osakola kanthu, koma pa mau anu ndidzaponya makoka. Ndipo pamene anacita ici, anazinga unyinji waukuru wa nsomba; ndipo makoka ao analinkung'ambika.

### Mateyu 20:30, 34

Ndipo onani, anthu akhungu awiri anakhala m'mphepete mwa njira; m'mene iwo anamva kuti Yesu analikupitirirapo, anapfuula nati, Muticitire ife cifundo, Inu Mwana wa Davide. . . Ndipo Yesu anagwidwa ndi cifundo, nakhudza maso ao; ndipo pomwepo anapenyanso, namtsata Iye.

### Akolose 1:16

Pakuti mwa Iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yacifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalengedwa mwa Iye ndi kwa Iye.

### Aroma 14:9

Pakuti, cifukwa ca ici Kristu adafera, nakhalanso ndi moyo, kuti Iye akakhale Ambuye wa akufa ndi wa amoyo.

### Yohane 1:3

Zonse zinalengedwa ndi Iye; ndipo kopanda Iye sikunalengedwa kanthu kali konse kolengedwa.

### Ahebri 1:2

Mulungu . . . koma pakutha pace pa masiku ano analankhula ndi ife ndi Mwana amene anamuika wolowa nyumba wa zonse, mwa Iyenso analenga maiko ndi am'mwamba omwe.

### Macitidwe A Atumwi 2:36

Pamenepo lizindikiritse ndithu banja liri lonse la Israyeli, kuti Mulungu anamuyesa Ambuye ndi Kristu, Yesu amene inu munampacika.

### 1 Akorinto 1:9

Mulungu ali wokhulupirika amene munaitanidwa mwa Iye, ku ciyanjano ca Mwana wace Yesu Kristu, Ambuye wathu.

Aroma 2:16
Tsiku limene Mulungu adzaweruza ndi Yesu Kristu zinsinsi za anthu, monga mwa uthenga wanga wabwino.

2 Timoteo 4:1
Ndikucitira umboni pamaso pa Mulungu ndi Kristu Yesu, amene adzaweruza amoyo ndi akufa, ndi pa maonekedwe ace ndi ufumu wace.

Macitidwe A Atumwi 10:42
Ndipo anatilamulira ife tilalikire kwa anthu, ndipo ticite umboni kuti Uyu ndiye amene aikidwa ndi Mulungu akhale woweruza amoyo ndi akufa.

Mateyu 25:32
Ndipo adzasonkhanidwa pamaso pace anthu a mitundu yonse; ndipo Iye adzalekanitsa iwo wina ndi mnzace, monga mbusa alekanitsa nkhosa ndi mbuzi.

Yohane 5:22
Pakuti Atate saweruza munthu ali yense, koma anapereka kuweruza konse kwa Mwana.

Aroma 14:10
Koma iwe uweruziranji mbale wako? kapena iwenso upeputsiranji mbale wako? pakuti ife tonse tidzaimirira ku mpando wakuweruza wa Mulungu.

Yohane 10:9

Ine ndine khomo; ngati wina alowa ndi Ine, adzapulumutsidwa, nadzalowa, nadzaturuka, nadzapeza busa.

Yohane 14:6

Yesu ananena naye, Ine ndine njira, ndi coonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine.

Macitidwe A Atumwi 4:12

Ndipo palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo.

Yohane 8:24

Cifukwa cace ndinati kwa inu, kuti mudzafa m'macimo anu, pakuti ngati simukhulupirira kuti Ine ndine, mudzafa m'macimo anu.

Ahebri 5:9

Ndipo pamene anakonzeka wamphumphu anakhala kwa onse akumvera Iye cifukwa ca cipulumutso cosatha.

Ahebri 7:25

Kucokera komweko akhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa Iye, popeza ali nao moyo wace cikhalire wa kuwapembedzera iwo.

Akolose 1:12-14

Ndi kuyamika Atate, amene anatiyeneretsa ife kulandirana nao colowa ca oyera mtima m'kuunika; amene anatilanditsa ife ku ulamuliro wa mdima, natisunthitsa kutilowetsa m'ufumu wa Mwana wa cikondi cace; amene tiri nao maomboledwe mwa Iye, m'kukhululukidwa kwa zocimwa zathu.

Luka 19:10

Pakuti Mwana wa munthu anadza kufunafuna ndi kupulumutsa cotayikaco.

1 Akorinto 1:30

Koma kwa Iye muli inu mwa Kristu Yesu, amene anayesedwa kwa ife nzeru ya kwa Mulungu, ndi cilungamo ndi ciyeretso ndi ciombolo.

Cibvumbulutso 5:9

Ndipo ayimba nyimbo yatsopano, ndi kunena, Muyenera kulandira bukulo, ndi kumasula zizindikilo zace; cifukwa mwaphedwa, ndipo mwagulira Mulungu ndi mwazi wanu anthu a mafuko onse, ndi manenedwe onse, ndi mitundu yonse.

Tito 2:14

Amene anadzipereka yekha m'malo mwa ife, kuti akatiombole ife ku zoipa zonse, nakadziyeretsere yekha anthu akhale ace eni eni, acangu pa nchito zokoma.

Aefeso 1:7

Tiri ndi maomboledwe mwa mwazi wace, cikhululukiro ca zocimwa, monga mwa kulemera kwa cisomo cace.

1 Yohane 1:7

Koma ngati tiyenda m'kuunika, monga Iye ali m'kuunika, tiyanjana wina ndi mnzace, ndipo mwazi wa Yesu Mwana wace utisambitsa kuticotsera ucimo wonse.

1 Petro 1:18, 19

Podziwa kuti simunaomboledwa ndi zobvunda, golidi ndi siliva, kusiyana nao makhalidwe anu acabe ocokera kwa makolo anu; koma ndi mwazi wa mtengo wace wapatali monga wa mwana wa nkhosa wopanda cirema, ndi wopanda banga, ndiwo mwazi wa Kristu.

Ahebri 9:14

Koposa kotani nanga mwazi wa Kristu amene anadzipereka yekha wopanda cirema kwa Mulungu mwa Mzimu wosatha, udzayeretsa cikumbu mtima canu kucisiyanitsa ndi nchito zakufa, kukatumikira Mulungu wamoyo?

Aroma 5:9

Ndipo tsono popeza inayesedwa olungama ndi mwazi wace, makamaka ndithu tidzapulumuka mkwiyo wa Mulungu mwa Iyeyo.

**Aroma 5:1**

**Popeza tsono tayesedwa olungama ndi cikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Kristu.**

**Yohane 20:31**

**Koma zalembedwa izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupira mukhale nao moyo m'dzina lace.**

**Aefeso 2:8, 9**

**Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu; cosacokera kunchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense.**

**1 Yohane 5:4**

**Pakuti ciri conse cabadwa mwa Mulungu cililaka dziko lapansi; ndipo ici ndi cilako tililaka naco dziko lapansi, ndico cikhulupiriro cathu.**

**Yohane 6:28, 29**

**Pamenepo anati kwa Iye, Ticite ciani, kuti ticite nchito za Mulungu? Yesu anayankha nati kwa iwo, Nchito ya Mulungu ndi iyi, kuti mukhulupirire Iye amene Iyeyo anamtuma.**

**Agalatiya 5:6**

**Pakuti mwa Kristu Yesu kapena mdulidwe kapena kusadulidwa kulibe mphamvu; komatu cikhulupiriro cakucititsa mwa cikondi.**

### Masalmo 108:4

Pakuti cifundo canu ncacikuru kupitirira kumwamba, Ndi coonadi canu kufikira mitambo.

### Tito 3:5

Zosati zocokera m'nchito za m'cilungamo, zimene tidazicita ife, komatu monga mwa cifundo cace anatipulumutsa ife, mwa kutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwe a Mzimu Woyera.

### Mika 7:18

Ndani Mulungu wofanana ndi Inu, wakukhululukira mphulupulu, wakupitirira zolakwa za otsala a colowa cace? sasunga mkwiyo wace ku nthawi yonse popeza akondwera naco cifundo.

### Maliro 3:22, 23

Cifukwa cakusathedwa ife ndico cifundo ca Yehova, pakuti cisoni cace sicileka; Cioneka catsopano m'mawa ndi m'mawa; mukhulupirika ndithu.

### Masalmo 103:11

Pakuti monga m'mwamba mutalikira ndi dziko lapansi, Motero cifundo cace cikulira iwo akumuopa Iye.

### Masalmo 103:17

Koma cifundo ca Yehova ndico coyambira nthawi yosayamba kufikira nthawi yosatha kwa iwo akumuopa Iye, Ndi cilungamo cace kufikira kwa ana a ana.

Cibvumbulutso 22:17
Ndipo Mzimu ndi mkwatibwi anena, Idzani. Ndipo wakumva anene, Idzani. Ndipo wakumva ludzu adze; iye wofuna, atenge madzi a moyo kwaulere.

Yohane 7:37
Koma tsiku lomariza, lalikurulo la phwando, Yesu anaimirira napfuula, ndi kunena, Ngati pali munthu akumva ludzu, adze kwa Ine, namwe.

Yesaya 55:1
Inu nonse, inu akumva ludzu, idzani kumadzi; ndi osowa ndarama idzani inu mugule mudye; inde idzani, mugule vinyo ndi mkaka opanda ndarama ndi opanda mtengo wace.

Yesaya 1:18
Tiyeni, tsono, tiweruzane, ati Yehova; ngakhale zoipa zanu ziri zofiira, zidzayera ngati matalala; ngakhale ziri zofiira ngati kapezi, zidzakhala ngati ubweya wa nkhosa, woti mbu.

2 Akorinto 5:20
Cifukwa cace tiri atumiki m'malo mwa Kristu, monga ngati Mulungu alikudandaulira mwa ife; tiumiriza inu m'malo mwa Kristu, yanjanitsidwani ndi Mulungu.

### 1 Yohane 3:10

M'menemo aoneka ana a Mulungu, ndi ana a mdierekezi: yense wosacita cilungamo siali wocokera mwa Mulungu; ndi iye wosakonda mbale wace.

### Aroma 8:14, 15

Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu. Pakuti inu simunalandira mzimu wa ukapolo kucitanso mantha; koma munalandira mzimu wa umwana, umene tipfuula nao, kuti, Abba, Atate.

### Afilipi 2:15

Kuti mukakhale osalakwa ndi oona, ana a Mulungu opanda cirema pakati pa mbadwo wokhotakhota ndi wopotoka, mwa iwo amene muonekera monga mauniko m'dziko lapansi.

### Yohane 1:12

Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lace.

### 2 Akorinto 6:17, 18

Cifukwa cace, Turukani pakati pao, ndipo patukani, ati Ambuye, Ndipo musakhudza kanthu kosakonzeka; Ndipo Ine ndidzalandira inu, Ndipo ndidzakhala kwa inu Atate, Ndi inu mudzakhala kwa Ine ana amuna ndi akazi, anena Ambuye Wamphamvuyonse.

Miyambo 23:31, 32

Usayang'ane pavinyo alikufiira. Alikung'azimira m'cikho. Namweka mosalala. Pa citsiriziro cace aluma ngati njoka, Najompha ngati mamba.

Yesaya 5:11

Tsoka kwa iwo amene adzuka m'mamawa kuti atsate zakumwa zaukali; amene acezera usiku kufikira vinyo awaledzeretsa!

Agalatiya 5:19-21

Ndipo nchito za thupi zionekera, ndizo dama, codetsa, kukhumba zonyansa, kupembedza mafano, nyanga madano, ndeu, kaduka, zopsa mtima, zotetana, magawano, mipatuko, njiru, kuledzera, mcezo, ndi zina zotere; zimene ndikucenjezani nazo, monga ndacita, kuti iwo akucitacita zotere sadzalowa Ufumu wa Mulungu.

Aroma 13:13, 14

Tiyendeyende koyenera, monga usana; si m'madyerero ndi kuledzera ai, si m'cigololo ndi conyansa ai, si mu ndeu ndi nkhwidzi ai. Koma bvalani inu Ambuye Yesu Kristu, ndipo musaganizire za thupi kucita zofuna zace.

Miyambo 20:1

Vinyo acita ciphwete, cakumwa caukali cisokosa; Wosocera nazo alibe nzeru.

### Mateyu 22:37, 38

Ndipo Yesu anati kwa iye, Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse. Ili ndilo lamulo lalikuru ndi loyamba.

### Marko 10:17-22

. . . namgwadira Iye, namfunsa, Mphunzitsi wabwino, ndidzacita ciani kuti ndilandire moyo wosatha? Ndipo Yesu anati kwa iye, Undicha Ine wabwino bwanji? palibe wabwino koma mmodzi, ndiye Mulungu. Udziwa malamulo: Usaphe, Usacite cigololo, Usabe, Usacite umboni wakunama, Usanyenge, Lemekeza atate wako ndi amako. Ndipo iye anati kwa Iye, Mphunzitsi, zonsezi ndinazisunga kuyambira ndiri mwana. Ndipo Yesu anamyang'ana, namkonda, nati kwa iye, Cinthu cimodzi cikusowa: pita, gulitsa zonse uli nazo, nuzipereke kwa anthu aumphawi, ndipo cuma udzakhala naco m'mwamba; ndipo ukadze kuno, unditsate Ine. Koma nkhope yace inagwa pa mau awa, ndipo anacoka iye wacisoni; pakuti anali mwini cuma cambiri.

### Miyambo 16:25

Iripo njira yooneka kwa mwamuna ngati yoongoka, Koma matsiriziro ace ndi njira za imfa.

Yakobo 1:22

Khalani akucita mau, osati akumva okha, ndi kudzinyenga nokha.

1 Akorinto 6:9, 10

Kapena simudziwa kuti osalungama sadzalandira ufumu wa Mulungu? Musasoceretsedwe; adama, kapena opembedza mafano, kapena acigololo, kapena olobodoka ndi zoipa, kapena akudziipsa ndi amuna, kapena ambala, kapena osirira, kapena oledzera, kapena olalatira, kapena olanda, sadzalowa Ufumu wa Mulungu.

Aefeso 5:6

Asakunyengeni inu munthu ndi mau opanda pace, pakuti cifukwa ca izi umadza mkwiyo wa Mulungu pa ana a kusamvera.

1 Yohane 3:7, 8a

Tiana, munthu asasokeretse inu; iye wakucita colungama ali wolungama, monga Iyeyu ali wolungama: iye wocita cimo ali wocokera mwa mdierekezi, cifukwa mdierekezi amacimwa kuyambira paciyambi.

Agalatiya 6:3

Pakuti ngati wina ayesa ali kanthu pokhala ali cabe, adzinyenga yekha.

Agalatiya 6:7

Musanyengedwe; Mulungu sanyozeka; pakuti cimene munthu acifesa, cimenenso adzacituta.

Aroma 8:6
Pakuti cisamaliro ca thupi ciri imfa; koma cisamaliro ca mzimu ciri moyo ndi mtendere.

Ezekieli 18:20
Moyo wocimwawo ndiwo udzafa; mwana sadzasenza mphulupulu za atate wace, ndi atate sadzasenza mphulupulu za mwana; cilungamo ca wolungama cidzamkhalira, ndi coipa ca woipa cidzamkhalira.

Yakobo 1:15
Pamenepo cilakolakoco citaima, cibala ucimo; ndipo ucimo, utakula msinkhu, ubala imfa.

Aroma 5:12
Cifukwa cace, monga ucimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu mmodzi, ndi imfa mwa ucimo; cotero imfa inafikira anthu onse, cifukwa kuti onse anacimwa.

Luka 15:32
Koma kudayenera kuti tisangalale ndi kukondwerera: cifukwa mng'ono wako uyu anali wakufa ndipo ali ndi moyo; anatayika, ndipo wapezeka.

Miyambo 11:19
Wolimbikira cilungamo alandira moyo; Koma wolondola zoipa adzipha yekha.

### Yohane 11:43, 44

Ndipo m'mene adanena izi, anapfuula ndi mau akuru, Lazaro, turuka. Ndipo womwalirayo anaturuka womangidwa miyendo ndi manja ndi nsaru za kumanda; ndi nkhope yace inazingidwa ndi mlezo. Yesu ananena nao, Mmasuleni iye, ndipo mlekeni amuke.

### Luka 7:14, 15a

Ndipo anayandikira, nakhudza cithatha; ndipo akumnyamulawo anaima. Ndipo Iye anati, Mnyamata iwe, ndinena ndi iwe, Tauka. Ndipo wakufayo anakhala tsonga, nayamba kulankhula.

### Cibvumbulutso 1:18

Ndi Wamoyoyo; ndipo ndinali wakufa, ndipo taona, ndiri wamoyo kufikira nthawi za nthawi, ndipo ndiri nazo zofungulira za imfa ndi Hade.

### Yohane 10:17, 18

Cifukwa ca ici Atate andikonda Ine, cifukwa nditaya Ine moyo wanga, kuti ndikautengenso. Palibe wina andicotsera uwu, koma ndiutaya Ine ndekha. Ndiri nayo mphamvu yakuutaya, ndi mphamvu ndiri nayo yakuutenganso; lamulo ili ndinalandira kwa Atate wanga.

### Deuteronomo 5:7-21

Usakhale nayo milungu yina koma Ine ndekha.

Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena cifaniziro ciri conse ca zinthu za m'thambo la kumwamba, kapena za m'dziko lapansi, kapena za m'madzi a pansi pa dziko; usazipembedzere izo, usazitumikire izo. . .

Usachule dzina la Yehova Mulungu wako pacabe; cifukwa Yehova sadzamuyesa iye wosacimwa amene achula pacabe dzina lacelo.

Samalira tsiku la Sabata likhale lopatulika, monga Yehova Mulungu wako anakulamulira. Masiku asanu ndi limodzi uzigwiritsa nchito, ndi kucita nchito zako zonse; koma tsiku lacisanu ndi ciwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako. . .

Lemekeza atate wako ndi amako, monga Yehova Mulungu wako anakulamulira. . .

Usaphe.

Usacite cigololo.

Usabe.

Usamnamizire mnzako.

Usasirire mkazi wace wa mnzako; usakhumbe nyumba yace ya mnzako, munda wace, kapena wanchito wace wamwamuna, ka-

pena wanchito wace wamkazi, ng'ombe yace, kapena buru wace, kapena kanthu kali konse ka mnzako.



Luka 8:17

Pakuti palibe cinthu cobisika, cimene sicidzakhala coonekera; kapena cinsinsi cimene sicidzadziwika ndi kubvumbuluka.

Yeremiya 23:24

Kodi munthu angathe kubisala mobisika kuti ndisamuone iye? ati Yehova. Kodi Ine sindidzala kumwamba ndi dziko lapansi? ati Yehova.

Miyambo 15:3

Maso a Yehova ali ponseponse, Nayang'anira oipa ndi abwino.

Masalmo 139:8, 12

Ndikakwera kumka kumwamba, muli komweko; Kapena ndikadziyalira ku Gehena, taonani, muli komweko. . . Ungakhale mdimạ sudetsa pamaso panu, Koma usiku uwala ngati usana: Mdima ukunga kuunika.

Yobu 34:21, 22

Pakuti maso ace ali pa njira ya munthu ali yense, Napenya moponda mwace monse. Palibe mdima kapena mthunzi wa imfa, Kuti ocita zopanda pace abisaleko.

Masalmo 9:17

Oipawo adzabwerera kumanda, Inde amitundu onse akuiwala Mulungu.

Mateyu 18:8

Ndipo ngati dzanja lako, kapena phazi lako likukhumudwitsa iwe, ulidule, nulitaye; nkwabwino, kuti ulowe m'moyo wopunduka dzanja kapena phazi, koposa kuponyedwa m'moto wa nthawi zonse, uli ndi manja awiri kapena mapazi awiri.

Mateyu 13:41, 42

Mwana wa munthu adzatuma angelo ace, ndipo iwo adzasonkhanitsa pamodzi, ndi kucotsa mu Ufumu wace zokhumudwitsa zonse, ndi anthu akucita kusayeruzika, ndipo adzawataya iwo m'ng'anjo yamoto; kumeneko kudzakhala kulira ndi kukukuta mano.

Mateyu 25:46

Ndipo amenewa adzacoka kumka ku cilango ca nthawi zonse; koma olungama ku moyo wa nthawi zonse.

2 Petro 3:7

Koma miyamba ndi dziko la masiku ano, ndi mau omwewo zaikika kumoto, zosungika kufikira tsiku la ciweruzo ndi ciononngeko ca anthu osapembedza.

Macitidwe A Atumwi 17:31
Cifukwa anapangira tsiku limene adzaweruza dziko lokhalamo anthu m'cilungamo, ndi munthu amene anamuikiratu; napatsa anthu onse citsimikizo, pamene anamuukitsa Iye kwa akufa.

1 Yohane 4:17
M'menemo cikondi cathu cikhala cangwiro kuti tikhale nako kulimbika mtima m'tsiku la mlandu; cifukwa monga Iyeyu ali, momwemo tiri ife m'dziko lino lapansi.

2 Akorinto 5:10
Pakuti ife tonse tiyenera kuonetsedwa ku mpando wa kuweruza wa Kristu, kuti yense alandire zocitika m'thupi, monga momwe anacita, kapena cabwino kapena coipa.

Ahebri 9:27
Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa, ciweruziro.

Aroma 14:12
Cotero munthu ali yense wa ife adzadziwerengera mlandu wace kwa Mulungu.

2 Petro 2:9
Ambuye adziwa kupulumutsa opembedza poyesedwa iwo, ndi kusunga osalungama kufikira tsiku loweruza akalangidwe.

### 2 Akorinto 9:15

Ayamikike Mulungu cifukwa ca mphatso yace yace yosatheka kuneneka.

### 1 Petro 5:5b

. . . pakuti Mulungu akaniza odzikuza, koma apatsa cisomo kwa odzicepetsa.

### Aroma 5:15

Koma mphatso yaulere siilingana ndi kulakwa. Pakuti ngati ambiriwo anafa cifukwa ca kulakwa kwa mmodziyo, makamaka ndithu cisomo ca Mulungu, ndi mphatso yaulere zakucokera ndi munthu mmodziyo Yesu Kristu, zinacurukira anthu ambiri.

### 2 Akorinto 8:9

Pakuti mudziwa cisomo ca Ambuye wathu Yesu Kristu, kuti, cifukwa ca inu anakhala wosauka, angakhale anali wolemera, kuti inu ndi kusauka kwace mukakhale olemera.

### Macitidwe A Atumwi 4:33

Ndipo atumwi anacita umboni ndi mphamvu yaikulu za kuuka kwa Ambuye Yesu; ndipo panali cisomo cacikuru pa iwo onse.

### Aroma 9:16

Cotero sicifuma kwa munthu amene afuna, kapena kwa iye amene athamanga, koma kwa Mulungu amene acitira cifundo.

Macitidwe A Atumwi 3:19

Cifukwa cace lapani, bwererani kuti afafanizidwe macimo anu, kotero kuti zidze nyengo zakutsitsimutsa zocokera ku nkhope ya Ambuye.

Luka 13:3

Ndinena kwa inu, Iaitu; koma ngati inu simutembenuka mtima, mudzaonongeka nonse momwemo.

Macitidwe A Atumwi 17:30

Nthawi za kusadziwako tsono Mulungu analekerera; koma tsopanotu alinkulamulira anthu onse ponse ponse atembenuke mtima.

Ezekieli 18:31

Tayani, ndi kudzicotsera zolakwa zanu zonse zimene munalakwa nazo, ndi kudzifunira mtima watsopano, ndi mzimu watsopano; pakuti mudzaferanji inu, nyumba ya Israyeli?

2 Akorinto 7:10

Pakuti cisoni ca kwa Mulungu citembenuzira mtima kucipulumutso, cosamvetsanso cisoni; koma cisoni ca dziko lapansi cicita imfa.

Mateyu 3:2

Nanena, Tembenukani mitima; cifukwa Ufumu wa Kumwamba wayandikira.

Ezekieli 18:21
Koma woipayo akabwerera kusiya macimo ace onse adawacita nakasunga malemba anga onse, ndi kucita ciweruzo ndi cilungamo, adzakhala ndi moyo ndithu, sadzafa.

Macitidwe A Atumwi 5:31
Ameneyo Mulungu anamkweza ndi dzanja lace lamanja, akhale Mtsogoleri ndi Mpulumutsi, kuti apatse kwa Israyeli kulapa, ndi cikhululukiro ca macimo.

Cibvumbulutso 3:20
Taona, ndaima pakhomo, ndigogoda; wina akamva mau anga nakatsegula pakhomo, ndidzalowa kwa iye, ndipo ndidzadya naye, ndi iye ndi Ine.

Yesaya 55:7
Woipa asiye njira yace, ndi munthu wosalungama asiye maganizo ace, nabwere kwa Yehova; ndipo Yehova adzamcitira cifundo; ndi kwa Mulungu wathu, pakuti Iye adzakhululukira koposa.

Marko 2:5
Ndipo Yesu pakuona cikhulupiriro cao ananena ndi wodwala manjenje, Mwana, macimo ako akhululukidwa.

Yesaya 1:16

Sambani, dziyeretseni; cotsani macitidwe anu oipa pamaso panga; lekani kucita zoipa.

1 Yohane 2:15, 16

Musakonde dziko lapansi, kapena za m'dziko lapansi. Ngati wina akonda dziko lapansi, cikondi ca Atate siciri mwa iye. Pakuti ciri conse ca m'dziko lapansi, cilakolako ca thupi ndi cilakolako ca maso, matamandidwe a moyo, sizicokera kwa Atate, koma ku dziko lapansi.

Aefeso 5:11

Ndipo musayanjane nazo nchito za mdima zosabala kanthu, koma maka-makanso muzitsutse.

Akolose 3:2

Lingalirani zakumwamba osati za padziko ai.

Tito 2:11, 12

Pakuti caonekera cisomo ca Mulungu cakupulumutsa anthu onse, ndi kutiphunzitsa ife kuti, pokana cisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi, tikhale ndi moyo m'dziko lino odziletsa, ndi olungama, ndi opembedza.

Yakobo 4:4

Akazi acigololo inu, kodi simudziwa kuti ubwenzi wa dziko lapansi uli udani ndi Mulungu? Potero, iye amene afuna kukhala bwenzi la dziko lapansi adziika mdani wa Mulungu.

### Ezekieli 36:26

Ndipo ndidzakupatsani mtima watsopano, ndi kulonga m'kati mwanu mzimu watsopano; ndipo ndidzacotsa mtima wamwala m'thupi, ndi kukupatsani mtima wamnofu.

### Yohane 3:3

Yesu anayankha nati kwa iye, Indetu, indetu, ndinena ndi iwe, Ngati munthu sabadwa mwatsopano, sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu.

### 2 Akorinto 5:17

Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano.

### 1 Petro 1:23

Inu amene mudabadwanso, osati ndi mbeu yofeka, komatu yosaola, mwa mau a Mulungu amoyo ndi okhalitsa.

### 1 Yohane 5:18

Tidziwa kuti yense wobadwa kucokera mwa Mulungu sacimwa, koma iye wobadwa kucokera mwa Mulungu adzisunga yekha, ndipo woipayo samkhudza.

### 1 Yohane 2:29

Ngati mudziwa kuti ali wolungama, muzindikira kuti ali yensenso wakucita cilungamo abadwa kucokera mwa Iye.

Aefeso 2:1, 6

Ndipo inu, anakupatsani moyo, pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zocimwa zanu. . . . ndipo anatiukitsa pamodzi, natikhazikitsa pamodzi m'zakumwamba mwa Kristu Yesu.

Agalatiya 5:24

Koma iwo a Kristu Yesu adapacika thupi, ndi zokhumba zace, ndi zilakolako zace.

1 Petro 2:24

Amene anasenza macimo athu mwini yekha m'thupi mwace pamtanda, kuti ife, titafa kumacimo, titakhale ndi moyo kutsata cilungamo; ameneyo mikwingwirima yace munaciritsidwa nayo.

Akolose 3:1

Cifukwa cace ngati munaukitsidwa pamodzi ndi Kristu, funani zakumwamba, kumene kuli Kristu wokhala pa dzanja lamanja la Mulungu.

Aroma 6:2, 11

Ife amene tiri akufa ku ucimo, tidzakhala bwanji cikhalire m'memo? . . . Cotero inunso mudziwerengere inu nokha ofafa ku ucimo, koma amoyo kwa Mulungu mwa Kristu Yesu.

Akolose 3:3

Pakuti munafa, ndipo moyo wanu wabisika pamodzi ndi Kristu mwa Mulungu.

**Aroma 6:23**

Pakuti mphotho yace ya ucimo ndi imfa; koma mphatso yaulere ya Mulungu ndiyo moyo wosatha wa mwa Kristu Yesu Ambuye wathu.

**Yohane 3:36**

Iye amene akhulupirira Mwanayo ali nao moyo wosatha; koma iye amene sakhulupirira Mwanayo sadzaona moyo, koma mkwiyo wa Mulungu ukhala pa iye.

**Agalatiya 6:8**

Pakuti wakufesera kwa thupi la iye yekha, cocokera m'thupi adzatuta cibvundi; koma wakufesera kwa Mzimu, cocokera mu Mzimu adzatuta moyo wosatha.

**Yohane 5:24**

Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mau anga, ndi kukhulupirira Iye amene anandituma Ine, ali nao moyo wosatha, ndipo salowa m'kuweruza, koma wacokera kuimfa, nalowa m'moyo.

**Yohane 3:14, 15**

Ndipo monga Mose anakweza njoka m'cipululu, cotero Mwana wa munthu ayenera kukwezedwa; kuti yense wakukhulupira akhale nao moyo wosatha mwa Iye.

**Yohane 14:21**
Iye wakukhala nao malamulo anga, ndi kuwasunga, iyeyu ndiye wondikonda Ine; koma wondikonda Ine adzakondedwa ndi Atate wanga, ndipo Ine ndidzamkonda, ndipo ndidzadzionetsa ndekha kwa iye.

**Aroma 8:16**
Mzimu yekha acita umboni pamodzi ndi mzimu wathu, kuti tiri ana a Mulungu.

**Yesaya 32:17**
Ndi nchito ya cilungamo idzakhala mtendere; ndi zotsata cilungamo zidzakhala mtendere, ndi kukhulupirika ku nthawi zonse.

**Agalatiya 4:6**
Ndipo popeza muli ana, Mulungu anatumiza Mzimu wa Mwana wace alowe m'mitima yathu, wopfuula Abba, Atate.

**1 Yohane 4:13**
M'menemo tizindikira kuti tikhala mwa Iye, ndi Iye mwa ife, cifukwa anatipatsako Mzimu wace.

**1 Yohane 3:18, 19**
Tiana, tisakonde ndi mau, kapena ndi lilime, komatu ndi kucita ndi m'coonadi. Umo tidzazindikira kuti tiri ocokera m'coonadi, ndipo tidzakhazikitsa mtima wathu pamaso pace.

Yohane 17:13

Koma tsopano ndidza kwa Inu; ndipo izi ndilankhula m'dziko lapansi, kuti akhale naco cimwemwe canga cokwaniridwa mwa iwo okha.

Aroma 14:17

Pakuti ufumu wa Mulungu sukhala cakudya ndi cakumwa, koma cilungamo, ndi mtendere, ndi cimwemwe mwa Mzimu Woyera.

Masalmo 16:11

Mudzandidziwitsa njira ya moyo: Pankhope panu pali cimwemwe cokwanira; M'dzanja lanu lamanja muli zokondweretsa zomka muyaya.

Yesaya 12:3

Cifukwa cace mudzakondwera pakutunga madzi m'zitsime za cipulumutso.

Yohane 15:11

Izi ndalankhula ndi inu, kuti cimwemwe canga cikhale mwa inu, ndi kuti cimwemwe canu cidzale.

Agalatiya 2:20

Ndinapacikidwa ndi Kristu; koma ndiri ndi moyo; wosatinso ine ai, koma Kristu ali ndi moyo mwa ine; koma moyo umene ndiri nao tsopano m'thupi, ndiri nao m'cikhulupiriro ca Mwana wa Mulungu, amene anandikonda, nadzipereka yekha cifukwa ca ine.

### 1 Samueli 12:15

Koma mukapanda kumvera mau a Yehova, ndi kupikisana ndi lamulo la Yehova, dzanja la Yehova lidzatsutsana nanu, monga linatsutsana ndi makolo anu.

### Macitidwe A Atumwi 2:38

Koma Petro anati kwa iwo, Lapani, batizidwani yense wa inu m'dzina la Yesu Kristu kuloza ku cikhululukiro ca macimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.

### 2 Atesalonika 1:7-9

Ndi kwa inu akumva cisautso mpumulo pamodzi ndi ife, pa bvumbulutso la Ambuye Yesu wocokera Kumwamba pamodzi ndi angelo a mphamvu yace, m'lawi lamoto, ndi kubwezera cilango kwa iwo osamdziwa Mulungu, ndi iwo osamvera Uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu; amene adzamva cilango, ndico cionongeko cosatha cowasiyanitsa ku nkhope ya Ambuye, ndi ku ulemerero wa mphamvu yace.

### Aroma 6:16

Kodi simudziwa kuti kwa iye amene mudzipereka eni nokha kukhala akapolo ace akumvera iye, mukhalatu akapolo ace a yemweyo mulikumvera iye; kapena a ucimo kulinga kuimfa, kapena a umvero kulinga kucilungamo?

Afilipi 2:11

Ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Kristu ali Ambuye, kucitira ulemu Mulungu Atate.

Mateyu 10:32, 33

Cifukwa cace yense amene adzabvomereza Ine pamaso pa anthu, Inenso ndidzambvomereza iye pamaso pa Atate wanga wa Kumwamba. Koma yense amene adzandikana Ine pamaso pa anthu, Inenso ndidzamkana iye pamaso pa Atate wanga wa Kumwamba.

Aroma 10:9, 10

Kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka: pakuti ndi mtima munthu akhulupira kutengapo cilungamo; ndi m'kamwa abvomereza kutengapo cipulumutso.

1 Yohane 2:23

Yense wakukana Mwana, alibe Atate; wobvomereza Mwana ali ndi Atatenso.

Luka 9:26

Pakuti amene ali yense adzacita manyazi cifukwa ca Ine ndi mau anga, Mwana wa munthu adzacita manyazi cifukwa ca iye, pamene adzafika ndi ulemerero wace ndi wa Atate, ndi wa angelo oyera.

### Mateyu 4:1, 10, 11

Pamenepo Yesu anatengedwa ndi Mzimu kumka kucipululu kukayesedwa ndi mdierekezi. . . . Pomwepo Yesu ananena kwa iye, Coka Satana, pakuti kwalembedwa, Ambuye Mulungu wako udzamgwadira, Ndipo Iye yekha yekha udzamlambira. Pomwepo mdierekezi anamsiya Iye, ndipo onani, angelo anadza, namtumikira Iye.

### 1 Petro 5:8

Khalani odzisungira, dikirani; mdani wanu mdierekezi, monga mkango wobuma, ayendayenda ndi kufunafuna wina akamlikwire.

### Aefeso 6:11

Tabvalani zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoze kucirimika pokana macenjerero a mdierekezi.

### 2 Akorinto 2:11

Kuti asaticenjerere Satana; pakuti sitikhala osadziwa macenjerero ace.

### Macitidwe a Atumwi 26:18

Kukawatsegulira maso ao, kuti atembenuke kucokera kumdima, kulinga kukuunika, ndi kucokera ulamuliro wa Satana kulinga kwa Mulungu, kuti alandire iwo cikhululukiro ca macimo, ndi colowa mwa iwo akuyeretsedwa ndi cikhulupiriro ca mwa Ine.

### 2 Atesalonika 2:8

Ndipo pamenepo adzabvumbulutsidwa wosayeruzikayo, amene Ambuye Yesu adzamthera ndi mzimu wa pakamwa pace, nadzamuononga ndi maonekedwe a kudza kwace.

### 2 Akorinto 10:4

Pakuti zida za nkhondo yathu siziri za thupi, koma zamphamvu mwa Mulungu zakupasula malinga.

### Yakobo 4:7, 8a

Potero mverani Mulungu; koma kanizani mdierekezi, ndipo adzakuthawani inu. Yandikirani kwa Mulungu, ndipo adzayandikira kwa inu.

### Ahebri 2:14

Popeza tsono ana ndiwo a mwazi ndi nyama, Iyenso momwemo adalawa nao makhalidwe omwewo kuti mwa imfa akamuononge iye amene anali nayo mphamvu ya imfa, ndiye mdierekezi.

### Aroma 8:35, 37

Adzatisiyanitsa ndani ndi cikondi ca Kristu? nsautso kodi, kapena kupsinjika mtima, kapena kuzunza, kapena njala, kapena usiwa, kapena zoopsya kapena lupanga kodi? . . . Koma m'zonsezi, ife tilakatu, mwa Iye amene anatikonda.

**Agalatiya 5:22, 23a**

**Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, cikhulupiriro, cifatso, ciletso.**

**Yohane 13:35**

**Mwa ici adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli naco cikondano wina ndi mnzace.**

**1 Yohane 4:20**

**Munthu akati, kuti, Ndikonda Mulungu, nadana naye mbale wace, ali wabodza: pakuti iye wosakonda mbale wace amene wamuona, sakhoza kukonda Mulungu amene sanamuona.**

**Yohane 21:16**

**Ananena nayenso kaciwiri, Simoni mwana wa Yona, ukonda Ine kodi? Ananena ndi Iye, Inde, Ambuye; mudziwa kuti ndikukondani Inu. Ananena naye, Weta nkhosa zanga.**

**1 Akorinto 13:1**

**Ndingakhale ndilankhula malilime a anthu, ndi a angelo, koma ndiribe cikondi, ndikhala mkuwa woomba, kapena nguli yolira.**

**1 Yohane 3:14**

**Ife tidziwa kuti tacokera kuturuka muimfa kulowa m'moyo, cifukwa tikondana ndi abale. Iye amene sakonda akhala muimfa.**

Macitidwe A Atumwi 10:39-41

Ndipo ife ndife mboni za zonse adazicita m'dziko la Ayuda ndi m'Yerusalemu; amenenso anamupha, nampacika pamtengo. Ameneyo, Mulungu anamuukitsa tsiku lacitatu, nalola kuti aonetsedwe, si kwa anthu onse ai, koma kwa mboni zosankhidwiratu ndi Mulungu, ndiwo ife amene tinadya ndi kumwa naye pamodzi, atauka iye kwa akufa.

Yohane 20:26-28

Ndipo pakupita masiku asanu ndi atatu akuphunzira ace analinso m'nyumbamo, ndi Tomasi pamodzi nao. Yesu anadza, makomo ali citsekere, naimirira pakati, nati, Mtendere ukhale ndi inu. Pomwepo ananena kwa Tomasi, Bwera naco cala cako kuno, nuone manja anga; ndipo bwera nalo dzanja lako, nuliike ku nthiti yanga, ndipo usakhale wosakhulupira, koma wokhulupira. Tomasi anayankha nati kwa Iye, Ambuye wanga, ndi Mulungu wanga.

Marko 16:9

Ndipo pamene Iye adauka mamawa tsiku loyamba la sabata, anayamba kuonekera kwa Maliya wa Magadala, amene Iye adamturutsira ziwanda zisanu ndi ziwiri.

### Mateyu 16:21

Kuyambira pamenepo Yesu anayamba kuwalangiza ophunzira ace, kuti kuyenera Iye amuke ku Yerusalemu, kukazunzidwa zambiri ndi akuru, ndi ansembe akuru, ndi alembi; ndi kukaphedwa, ndi tsiku lacitatu kuuka kwa akufa.

### Yohane 5:25, 28, 29

Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti ikudza nthawi, ndipo iripo tsopano, imene akufa adzamva mau a Mulungu; ndipo iwo akumva adzakhala ndi moyo. . . Musazizwe ndi ici, kuti ikudza nthawi, imene onse ali m'manda adzamva mau ace, nadzaturukira, amene adacita zabwino, kukuuka kwa moyo; koma amene adacita zoipa kukuuka kwa kuweruza.

### Aroma 6:3-5

Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Kristu Yesu; tinabatizidwa mu imfa yace? Cifukwa cace tinaikidwa m'manda pamodzi ndi Iye mwa ubatizo kulowa muimfa; kuti monga Kristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemerero wa Atate, cotero ifenso tikayende m'moyo watsopano. Pakuti ngati ife tinakhala olumikizidwa ndi Iye m'cifanizidwe ca imfa yace, koteronso tidzakhala m'cifanizidwe ca kuuka kwace.

Luka 1:74, 75

Kutipatsa ife kuti titalanditsidwa ku dzanja la adani athu, Tidzamtumikira Iye, opanda mantha, M'ciyero ndi cilungamo pamaso pace, masiku athu onse.

2 Akorinto 7:1

Pokhala nao tsono malonjezano amenewa, okondedwa, tidzikonzere tokha kuleka codetsa conse ca thupi ndi ca mzimu, ndi kutsiriza ciyero m'kuopa Mulungu.

2 Timoteo 2:21

Ngati tsono munthu adziyeretsa yekha pa izi, adzakhala cotengera ca kuulemu, copatulidwa, coyenera kucita naco Mbuye, cokonzera nchito yonse yabwino.

1 Petro 1:2

Monga mwa kudziwiratu kwa Mulungu Atate, m'ciyeretso ca Mzimu, cocitira cimvero, ndi kuwaza kwa mwazi wa Yesu Kristu: Cisomo, ndi mtendere zicurukire inu.

1 Petro 1:15

Komatu monga Iye wakuitana inu ali woyera mtima, khalani inunso oyera mtima m'makhalidwe anu onse.

2 Timoteo 2:15

Ucite cangu kudzionetsera kwa Mulungu wobvomerezeka, wanchito wopanda cifukwa ca kucita manyazi, wolunjika nao bwino mau a coonadi.

Ahebri 13:12

Mwa ici Yesunso, kuti akayeretse anthuwo mwa mwazi wa Iye yekha, adamva cowawa kunja kwa cipata.

1 Yohane 1:9

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse.

Aefeso 1:4

Monga anatisankha ife mwa Iye, lisanakhazikike dziko lapansi, tikhale ife oyera mtima, ndi opanda cirema pamaso pace m'cikondi.

Mateyu 3:11

Inetu ndikubatizani inu ndi madzi kuloza ku kutembenuka mtima; koma Iye wakudza pambuyo panga, ali wakundiposa mphamvu, amene sindiyenera kunyamula nsapato zace: Iyeyu adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera ndi moto.

Yesaya 35:8

Ndipo kudzakhala khwalala kumeneko, ndi njira, ndipo idzachedwa njira yopatulika; audio sadzapita m'menemo; koma Iye adzakhala nao oyenda m'njira, ngakhale opusa, sadzasocera m'menemo.

**Macitidwe A Atumwi 13:52**
Ndipo akuphunzira anadzazidwa ndi cimwemwe ndi Mzimu Woyera.

**Luka 11:13**
Potero, ngati inu, okhala oipa, mudziwa kupatsa ana anu mphatso zabwino, koposa kotani nanga Atate wanu wa Kumwamba adzapatsa Mzimu Woyera kwa iwo akumpempha Iye?

**Aroma 8:9**
Koma inu simuli m'thupi ai, koma mumzimu, ngatitu Mzimu wa Mulungu akhalabe mwa inu. Koma ngati munthu alibe Mzimu wa Kristu, siali wace wa Kristu.

**Ezekieli 36:27**
Ndipo ndidzaika mzimu wanga m'kati mwanu, ndi kukuyendetsani m'malemba anga; ndipo mudzasunga maweruzo anga ndi kuwacita.

**Macitidwe A Atumwi 1:8a**
Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga. . .

**Macitidwe A Atumwi 4:31**
Ndipo m'mene adapemphera iwo, panagwedezeka pamalo pamene adasonkhanirapo; ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nalankhula mau a Mulungu molimbika mtima.

Cibvumbulutso 21:4

Ndipo adzawapukutira misozi yonse kuicotsa pamaso pao; ndipo sipadzakhalanso imfa; ndipo sipadzakhalanso maliro, kapena kulira, kapena cowawitsa; zoyambazo zapita.

1 Petro 4:12, 13

Okondedwa, musazizwe ndi mayesedwe amoto adakugwerani inu akhale cakukuyesani, ngati cinthu cacilendo cacitika nanu: koma popeza mulawana ndi Kristu zowawa zace, kondwerani; kutinso pa bvumbulutso la ulemerero wace mukakondwere kwakukurukuru.

Masalmo 34:18

Yehova ali pafupi ndi iwo a mtima wosweka, Apulumutsa iwo a mzimu wolapadi.

Yesaya 66:2

Pakuti zonsezi mkono wanga wazilenga, momwemo zonsezi zinaoneka, ati Yehova; koma ndidzayang'anira munthu uyu amene ali waumphawi, ndi wa mzimu wosweka, nanthunthumira ndi mau anga.

Masalmo 37:3

Khulupirira Yehova, ndipo cita cokoma; Khala m'dziko, ndipo tsata coonadi.

**Yesaya 43:2**

Pamene udulitsa pamadzi ndiri pamodzi ndi iwe; ndi pooloka mitsinje sidzakukokolola; pakupyola pamoto sudzapsya; ngakhale lawi silidzakutentha.

**Aroma 8:28**

Ndipo tidziwa kuti amene akonda Mulungu zinthu zonse zithandizana kuwacitira ubwino, ndiwo amene aitanidwa monga mwa kutsimikiza kwa mtima wace.

**1 Akorinto 10:13**

Sicinakugwerani inu ciyeso koma ca umunthu; koma Mulungu ali wokhulupirika, amene sadzalola inu kuyesedwa koposa kumene mukhosa; koma pamodzi ndi ciyeso adzaikanso populumukirapo, kuti mudzakhose kupirirako.

**Ahebri 2:18**

Pakuti popeza adamva zowawa, poyesedwa yekha, akhoza kuthandiza iwo amene ayesedwa.

**Aroma 16:20**

Ndipo Mulungu wa mtendere adzaphwanya Satana pansi pa mapazi anu tsopano lino. Cisomo ca Ambuye wathu Yesu Kristu cikhale ndi inu nonse.

**Masalmo 34:19**

Masautso a wolungama mtima acuruka: Koma Yehova amlanditsa mwa onsewa.

Cibvumbulutso 3:5

Iye amene alakika adzambveka motero zobvala zoyera; ndipo sindidzafafaniza ndithu dzina lace m'buku la moyo, ndipo ndidzambvomereza dzina lace pamaso pa Atate wanga, ndi pamaso pa angelo ace.

Cibvumbulutso 3:12

Iye wakulakika, ndidzamyesa iye mzati wa m'Kacisi wa Mulungu wanga, ndipo kuturuka sadzaturukamonso; ndipo ndidzalemba pa iye dzina la Mulungu wanga, ndi dzina la mzinda wa Mulungu wanga, la Yerusalemu watsopano, wotsika m'Mwamba, kucokera kwa Mulungu wanga; ndi dzina langa latsopano.

Cibvumbulutso 2:7

Iye wokhala nalo khutu amve cimene Mzimu anena kwa Mipingo. Kwa iye amene alakika ndidzampatsa kudya za ku mtengo wa moyo umene uli m'Paradaiso wa Mulungu.

Cibvumbulutso 3:21

Iye wakulakika, ndidzampatsa akhale pansi ndi Ine pa mpando wacifumu wanga, monga Inenso ndinalakika, ndipo ndinakhala pansi ndi Atate wanga pa mpando wacifumu wace.

### Mateyu 5:32

Koma Ine ndinena kwa inu, kuti yense wakucotsa mkazi wace, kosati cifukwa ca cigololo, amcititsa cigololo: ndipo amene adzakwata wocotsedwayo acita cigololo.

### Luka 16:18

Yense wakusudzula mkazi wace, nakwatira wina, acita cigololo; ndipo iye amene akwatira wosudzulidwayo, acita cigololo.

### Aroma 7:2, 3

Pakuti mkazi wokwatidwa amangidwa ndi lamulo kwa mwamuna wace wamoyo; koma mwamunayo akafa, iye amasulidwa ku lamulo la mwamunayo. Ndipo cifukwa cace, ngati iye akwatiwa ndi mwamuna wina, pokhala mwamuna wace wamoyo, adzanenedwa mkazi wacigololo; koma mwamunayo akafa, iye amasulidwa ku lamuloli; cotero sakhala wacigololo ngati akwatiwa ndi mwamuna wina.

### 1 Akorinto 7:10, 11

Koma okwatitsidwawo ndiwalamulira, si ine ai, koma Ambuye, kuti mkazi asasiye mwamuna, komanso ngati amsiya akhale osakwatiwa, kapena ayanjanitsidwenso ndi mwamunayo, ndipo mwamuna asalekane naye mkazi.

**Ndipo ndikapita kukakukonzerani inu malo, ndidzabweranso kudzakutengani, kuti inunso mukakhale kumene kuli Ine.**

**–Yohane 14:3**

**Pamenepo cizindikiro ca Mwana wa Munthu cidzaoneka kuthambo. Anthu a mitundu yonse ya pansi pano adzalira, ndipo adzaona Mwana wa Munthu akubwera pamitambo ndi ulemerero waukulu.**

**–Mateyu 24:30**

**Tsono ngati munthu acita manyazi ndi Ine ndiponso ndi mau anga pamaso pa anthu oipa a makono, amene sasamala za Mulungu, Mwana wa Munthu nayenso adzacita naye manyazi pamene adzafika pamodzi ndi angelo oyera, ali ndi ulemerero wa Atate ake.**

**–Marko 8:38**

**Pakuti Mwana wa Munthu adzabwera ndi angelo ake ndi ulemerero wa Atate ake, ndipo pomwepo adzabwezera aliyense molingana ndi zimene anacita. –Mateyu 16:27**

**Conco inunso khalani okonzeka, pakuti Mwana wa Munthu adzabwera panthawi imene simuyembekeza. –Luka 12:40**

**Za kuthambo ndi dziko lapansi zidzatha, koma mau anga sadzatha mphamvu konse.**
**–Luka 21:33**

**Pakuti mau a aneneri sanadze konse ndikufuna kwa munthu yekha, koma pamene Mzimu Woyera anawalankhulitsa, apo anthu analankhula mau ocokera kwa Mulungu. –2 Petro 1:21**

**Malembo onsewo anawauzira ndi Mulungu, ndipo amathandiza pakuphunzitsa coona, pakutsutsa zolakwa, pakukonza zolakwazo, ndiponso pakulangiza anthu za moyo wolungama.**
**–2 Timoteyo 3:16**

## PEMPHERA NDIPO KHULULUKIRANI

**Ncifukwa cake popemphera muziti, Atate athu a Kumwamba, dzina lanu lilemekezedwe. Ufumu wanu udze. Zimene Inu mufuna, zicitikenso pansi pano monga Kumwamba. Mutipatse lero cakudya cathu ca lero. Mutikhululukire ife macimo athu, monga ifenso takhululukira oticimwira. Ndipo musalole kuti tiyesedwe, koma mutipulumutse kwa Woipa uja. [Pakuti ufumu, mphamvu ndi ulemerero nzanu kwamuyaya. Amen.] Cifukwa ngati mukhululukira anthu zolakwa zao, Atate anu a Kumwamba adzakukhululukirani inunso. Koma ngati simukhululukira anthu zolakwa zao, Atate anunso sadzakukhululukirani zolakwa zanu.**
**–Mateyo 6:9-15**

# NJIRA YA MULUNGU YA CIPULUMUTSO

*Ndifuna Mpulumutsi.*

**Pakuti onse anacimwa, nalephera kufika ku ulemerero umene Mulungu anawakonzera.**
**–Aroma 3:23**

*Khristu anafera ine.*

**Pakuti Khristu mwini anafera macimo a anthu kamodzi kokha. Iye wolungama anatifera ife osalungama kuti atifikitse kwa Mulungu. –1 Petro 3:18a**

*Ndiyenera kulapa macimo anga.*

**Wobisa macimo ake sadzaona mwai; Koma wakuwabvomereza, nawasiya adzacitidwa cifundo. –Miyambo 28:13**

**Cifukwa cake lapani, bwererani kuti akufafanizireni macimo anu. –Macitidwe a Atumwi 3:19a**

*Ndiyenera Kulandira Yesu ndi Cikhulupiriro.*

**Komabe anthu onse amene anamlandira ndi kumkhulupirira, Iye anawapatsa mphamvu yokhala ana a Mulungu. –Yohane 1:12**

*Nditsimikiza ndiri naco Cipulumutso Canga.*

**Iye amene ali ndi Mwanayo, ali nawo moyo. –1 Yohane 5:12a**

**Zoonadi ndikukuuzani kuti munthu womva mau anga, nakhulupirira Iye amene ananditumа, ali nawo moyo wosatha. Iyeyo salangidwa, koma watuluka kale muimfa, ndipo walowa m'moyo. –Yohane 5:24b**

Published in numerous languages by World Missionary Press, Inc., as God supplies funds in answer to prayer. **For questions or more information by country, visit: www.wmp-contacts.org**

World Missionary Press
PO Box 120
New Paris, IN 46553-0120 USA
www.wmpress.org

3-23

Read booklets online or by App
www.wmp-readonline.org
9 Chichewa HFA